


# TIFUNSENI MAGANIZO ATHU

“Tikufuna Chitukuko Chimene Tikuchifuna Kwathu Kuno Chikwaniritsidwe.”

## Projekiti Ya Mpatamanga Damu, Malawi



### KUTI?:

Mtsinje wa Shire, mu maboma a Blantyre ndi Neno

### AKUPELEKA NDALAMA:

Boma la Malawi ndi ma banki othandiza chitukuko a IFC ndi World Bank

### AKUYANG'ANIRA NTCHITO YOKONZEKERA:

Boma la Malawi kudzera mwa dipatimenti yoona za magetsi

### AKUCHITA KAFUKUFUKU OSAMUTSA OKHUDZIDWA:

Mott Macdonald ndi C12 Consultants

### NTCHITO IMENE IGWIRIDWE:

Kumanga ma damu awiri opangira magetsi, kuunika mmene chilengedwe chikhudzidwire ndi damu'yi komanso kukonzekera ntchito yosamutsa okhudzidwa.



Boma la Malawi mothandizidwa ndi banki ya IFC ndi thandizo la ndalama lochokera ku World Bank likukonza ma pulani omanga ma damu awiri opangira magetsi.



Projekiti'yi ndi yomanga ma damu awiri opangira magetsi kuchokera ku mphamvu ya madzi pa mtsinje wa Shire mu maboma a Blantyre ndi Neno.



Ntchito yokonzekera projekiti'yi akuyang'anira ndi a dipatimenti yoona za magetsi. Boma la Malawi lalemba ntchito kampani ya Mott Macdonald amene nawonso alemba ntchito C12 Consultants kuti awunike mmene chilengedwe chikhudzidwire komanso kugwira ntchito yokonzekera kusamutsa okhudzidwa.

## PHINDU La Projekiti'yi



Kuchulutsa kwa mphamvu ya magetsi omwe akupangidwa ku Malawi



Anthu okhala m'midzi yozungulira adzakhala ndi mwayi opeza ntchito



Kutukula chuma cha dziko

## ZOYIPA zobwera kamba ka Projekiti'yi



Anthu adzaluza malo awo olima



Anthu adzaluza nyumba zawo zokhalamo



Manda adzasamutsidwa



Kufala kwa matenda opatsirana pogonana komanso kupatsidwa pakati kwa ana achichepele



Alimi azasowa kopezera ndalama komanso chakudya

Mu Okutobala 2020, **CHRR mothandizidwa ndi bungwe la IAP** adathandiza anthu okhudzidwa ndi **projekiti ya Mpatamanga damu** kutenga maganizo ndi nkhwawa zawo pa projekiti'yi, komanso maganizo awo pa njira zothandizira kuthetsa mavuto omwe akukumana nawo komanso omwe angabwere kamba ka projekiti'yi. Anthu 123 anatenga nawo mbali wa kafukufuku'yu. Mu March 2021, CHRR idakonzanso misonkhano ndi anthu okhudzidwa ndi projekiti'yi.

## Zina mwa zimene anthu adanena ndi izi:

0%



**Anthu onse okhudzidwa sanafunsidwe za maganizo awo pa projekiti'yi pamene ma pulani a projekiti'yi amapangidwa.**

“

Tinamva za projekiti'yi panthawi imene amapanga kafukufuku owona mmene anthu ndi chilengwe zikukhudzidwira.

”

70%



**70% ya okhudzidwa adalibe uthenga okwanira okhudza chitukukochi kuti athe kupereka maganizo awo.**

“

Projekiti'yi isanafike, madzi osefukira adagwetsa mulatho, a boma adabweretsa zida kuti mulatho'wo umangidwenso koma projetiki ya damu'yi idayimitsa ntchito yomanganso mulatho'wo.

”

76%



**76% ya okhudzidwa samadziwa kuti amene adziyendetsa projekiti'yi ndi ndani.**

“

Ndili ndi mafunso ambiri okhudza projekiti'yi ndi mmene itikhudziwe ife anthu ozungulira. Ndikupempha a ku boma kuti achititse misonkhano kuti tikambirane limodzi.

”

76%



**76% samadziwa kosiya madandaulo awo.**

“

A ku boma sanachititseko msonkhano m'mudzi wathu uno kuti atipatse ma uthenga oyenera a projekiti'yi.

”



## Zobwera Mtsogolo - Kafukufuku atatha, anthu okhudzidwa akupereka maganizo awo motere:

**Boma la Malawi** lifunse maganizo a anthu okhudzidwa pa ma pulani a projekiti'yi kuti athe kupereka maganizo a chitikuko chomwe akufuna m'midzi yawo.

**A dipatiment yooza za magetsi ngati oyang'anira ntchito yokonzekera awapatse anthu okhudzidwa ma uthenga oyenera okhudza projekiti'yi.**

**A dipatimenti yoona zamagetsi atsate ndondomeko zoyenera popanga ma pulani osamutsa anthu okhudzidwa.**

**A IFC ndi World Bank awonetsetse kuti ndalama zomwe akupereka ku projekiti'yi zisaphwanye ma ufulu a anthu ozungulira.**

Kafukufukuyu anachitidwa ngati mbali imodzi ya ntchito ya **Early Warning System** yofuna kuonetsetsa kuti midzi yokhudzidwa ndi chitikuko komanso mabungwe omwe amagwira nawo ntchito akudziwa zokhudza chitikuko chobwera m'midzi yawo chimene chingaphwanye ufulu wawo wa chibadwidwe ndi ufulu okhala ndi chilengedwe chabwino. Kuti mudziwe zambiri: [ews.rightsindevelopment.org](http://ews.rightsindevelopment.org)